




MUTU 10:

ZOZIZWITSA
NIDI MAFANIZO




KWINA KWAKE
KUDAALI MUDZI WA
ANTHU AKHATE...

MASIKU AMBIRI
APITAPO TSOPANO
NDISANADYE
CHILICHONSE.

UKUFA NGATI
SUPHUNZIRA KUDYA
MBEWA NDI TINYAMA
TINA. KUDYA ZIMENEZI
NDI NJIRA YOKHAYO
IMENE TINGAKHALIRE
NDI MOYO.

NDIYESA NDIKHALA
WOYAMBA KUFA NDINE.
CHAKA CHATHA CHOMWECHI
NDINALI MUNTHU WOLEMERA
KWAMBIRI; WOLEMEKEZEKA.
TANGOONANI MOMWE
NDILILI TSOPANO.

SUKULEMEKEZEKANSO
TSOPANO; NDIWE
WAKHATE, WOTAIDWA
KUNJA.




POYAMBIRIRA NDINALI NDI
CHIYEMBEKEZO CHOTI NDIDZACHIRA
NDI KUBWERERA KWA MKAZI WANGA NDI
ANA ANGA. KOMA NDAKHALA KUNO ZAKA
KHUMI TSOPANO, NDIPO PALIBE AMENE
NDAMUONA ATACHIRA NKUBWERERA
KUMUDZI WAO.



POYAMBA MKAZI WANGA
ANKANDIBWERETSERA ANA NDIPO
ANKAIMA PATALI NKUMAYANKHULA NANE.
KOMA KENAKA ANAYAMBA KUMABWERA
KAMODZI PAKAPITA NTHAWI YAITALI. NDIYE
KUTI ANA ANGA ANAKULA TSOPANO.
ATANDIONA SANGANDIZINDIKIRE. NDI
BWINO KUNGOFA BASI KUSIYANA
NKUMAZUNZIKA CHOTERE.

AAA, LEKA
KUDZIMVERA CHISONI.
PALIBE AMENE AMASAMALIRA,
NGAKHALE MULLINGU AMENE.
TIYENI TIZIPITA TIKAYESE
KUPEMPHAKO CHOTI
TIDYE.





TIPITA KU
MSEU WAUKULU
LERO. TIKAONE
NGATI ENA ANGATHE
KUTICHITIRAKO
CHIFUNDO.

NDI BWINO KUTI
TIYENDERE LIMODZI.
NDIKUONA ANTHU
AKHATE
PATSOGOLOPO.



**NDIKUONA
ANTHU APAULENDO
MUMSEUMU!**



**TAONANI! NDI
ANYAMATA OMWE
AJANSO.**

**CHOKANI KUNO,
ANTHU ODETSEDWA
AKHATE. PITANI KWINA
NDIPO MUKAFERE
KOMWEKO.**


**INU MPHUTSI
ZODETSEDWA!
MULINGU
AKUKULANGANI.**

**THAMANGANI!
THAMANGANI!**



ODETSEDWA!
ODETSEDWA,
TONSEFE NDIFE
ODETSEDWA.


NDI ANTHU
AKHATE. MUSALOLE
KUTI AKUYANDIKIRENI.
ANGAKUPATSIRENI
MATENDAWO.



TICHITIRENIKO
CHIFUNDO. TIPATSENIKO
CHAKUDYA, NGAKHALE
CHOHEPA, KUTI ALIYENSE
WA IFE ALUMEKO.

APATSENI
CHAKUDYA
CHILICHONSE
KUTI AZIPITA.

PITANI.
*INU ANTHU
ODETSEDWA!*



FUTUKANI KAYE
NDIPO CHAKUDYACHO
TICHISIYA PANO,
PANSI.

MUSAYANDIKIRE.
NDIYAMBE
NDACHOKA KAYE.



BURED!

SUNGIRENIKO!

CHAKLIDYA!

**MUSAMALIZE
CHONSE!**




**NDI
CHANGA!**

**IWE
CHINGU
BUDU!**

**INU
MULUNGU!**


**BURED!
BURED!**



KUKUBWERA
GULU LALIKULU
LA ANTHU
OYENDA MU
MSEU.

TICHENJERE
CHIFUKWA
NDI ANTHU
AMBIRI ZEDI.

NDIPO
ONSEWO NDI
AMLUNA.



AMENEYO NDI YESU
WA KU NAZARETI.
NDINAMUONAPO
KAMODZI NDISANAYAMBE
KUDWALA MATENDAWA.
IYEYU NDI AMENE
AMACHIRITSA ANTHU.

AMATI NDI WOCHOKERA
KWA MULLINGU. AMATI
IYEYU NDI ATATE NDI
AMODZI. NDIDAMUONA
AKUCHIRITSA MUNTHU
WAKHUNGU NDIPONSO
MUNTHU WOLLUMALA.



**YESU!
TITHANDIZENI!**

**AMBUYE, NDI
ANTHU AKHATE.**

**MUSALOLE KUTI
AKUYANDIKIRENI**



MUFUNA
NDIKUCHITIRENI
CHIYANI?

MUTICHITIRE
CHIFUNDO NDIPO
MUTICHIRITSE.

NGATI MUFUNA,
MUKHOZA
KUNDICHIRITSA.



MUSANDIGWIRE.

MUSADE NKHAWA.
PITANI KU NYUMBA YA
MULINGU NDIPO MUKADZIONETSE
KWA WANSEMBE. AKAONA KUTI
MWACHIRA NDIPO AKAKULOLANI
KUBWERERA KUMUDZI KWANU;
KU MABANJA ANU.



AKUTI
TACHIRITSIDWA.

AKATITHAMAN
GITSA
TISANAYANDIK
IRE NYUMBA
YA MULLINGU.

INE
NDICHITA
MONGA
WANENERA.

INENSO
NDICHITA NGATI
IWEYO. TIYE
TIZIPITA.

LUKA 17:11-14



YESU ANATI
TACHIRITSIDWA.



NDIKUPEZA
BWINO.



TIKUSINTHIKA!






**KHUNGU LANGA
LACHIRITSIDWA!**

**YESU NDIYE
WACHITA ZIMENEZI!
MWACHIRA!**

**SINDINUNSO
ONYANSA!**

**NDIPITE KWA
MKAZI WANGA!**



WODALITSIKA NDINU,
MWANA WA MULLINGU, MFUMU
YA ISRAELE. MWANDIPATSANSO
MOYO WANGA. MULLINGU NDI
WACHIFUNDO NDI WACHISOMO.

KODI ANACHIRITSIDWA AJA SI
ANTHU KHUMI? KOMA MMODZI YEKHA
NDIYE WABWERA KUDZATHOKOZA,
KOMANSO SI MYUDA. NDI
MSAMARIYA.

LUKA 17:14-19

MUNTHU WINA ANAFUNSA
YESU NGATI ANTHU
AMBIRI AKALOWA KU
MOYO WOSATHA. YESU
ANAYANKHA KUTI:

MOYO WOSATHA



NDIKUKUZANI, NJIRA
YA KU MOYO WOSATHA NDI
YOVUTA KOMANSO NDI
YOPAPATIZA NDIPO NDI ANTHU
OCHEPA AMENE AMAIPEZA. KOMA
NJIRA YA KU CHIONONGEKO NDI
YOTAKATA NDIPO NDI YODZALA
NDI ANTHU OPITA KU
CHIONENGEKO CHOSATHA.



YESETSANI KULOWA
PA CHIPATA CHOPAPATIZA,
PAKUTI AMBIRI ADZAFUNAFUNA
KULOWA KU MOYO WOSATHA KOMA
ADZALEPHERA. TSIKU LACHIONONGEKO
LIKADZAFIKA, ANTHU AMBIRI
ADZADANDAULIRA MULLINGU, KUNENA
KUTI, "AMBUYE INETU NDINALI WANU.
NDINALI MUNTHU WOPEMBEDZA.
NDINKASALA ZAKUDYA KOMANSO
NDINKAPEMPHERA. NDINKAPEREKA
NDALAMA ZOTHANDIZIRA
CHIPEMBEDZO. NDINKANENERA
M'DZINA LANU NDI KUCHOTSA
ZIWANDA."



**PAMENEPO INE NDIDZATI
KWA IWO, "SINDIKUDZIWANI.
CHOKANI KWA INE, INU
ANTHU OTEMBEREREDWA,
PITANI KU MOTO WOSATHA.
KUMENECO MUDZALIRA NDI
KUKUKUTA MANO."**

**KUMENECO NDI
KUMALO KUMENE MIZIMU YAO
SIKUFANDA NIPO MOTO SUZIMA.
UTSI WA MAZUNZO UDZAKHALA
UKUPITA KUMWAMBA MPAKA
KALEKALE.**

**MATEYU 7:13-14, 22-23;
CHIVUMBULUTSO 14:11**



YESU ANANENA
NTHANO:

PANALI MUNTHU WINA AMENE
ANKAVALA ZOVALA ZOKONGOLA
NDIPONSO ANKADYA ZAKUDYA ZONONA
TSIKU NDI TSIKU. ANALI MUNTHU
WACHILINGAMO NDI WABWINO NDITHU,
KOMA ANKANGOLABADA
ZA IYE YEKHA.

ANALI NDI
NDALAMA
ZAMBIRI NDIPO
ANKANGOLEMERE
RALEMERERA.

TENGANI MAKOMBO
AWA NDIPO MUKAWAPEREKE
KWA MUNTHU WOPEMPHA
AMENE ALI PA CHIPATA PAJA.
NDINE MUNTHU WACHIFUNDO
KWAMBIRI NDIPO NDIMAFUNIRA
ENA ZABWINO.



INDE BWANA,
NDIKHULLUPIRIRA KUTI
AKAYAMIKA KWAMBIRI
CHIFUKWA CHA
CHIMENECHI.



ABWANA AMATI
NDIKUPATSENI
MAKOMBOWA.

**AMBLIYE
ALEMEKEZEKE!**
MULINGU AMASAMALA
ANTHU AKE. CHAKUDYACHI
CHINDIKWANIRA.
MUKANDITHOKOZEREKO
KWA ABWANA ANU.

NDILI NDI
CHUMA CHAMBIRI,
PAFUNIKA NKHOKWE
ZINA ZOKULIRAPO
KUTI ZITHE KUSUNGA
CHUMACHI.



NDIPO USIKU WOMWEWO
MNGELO WA IMFA ANABWERA.

**WOPUSA IWE.
USIKU WOMWE LINO
LUKIFA NDIPO LUKATULA
NTCHITO ZAKO PAMASO
PA MULLINGU.**


MAYOO! GWIRANI
APA! OOOO-KHUU

“KUNAIIKA KUTI
MUNTHU AZIFA KAMODZI
NDIPO AKAFI TERO
AWERUZIDWE.”

LUKA 16:19-22;
AHEBRI 9:27

PALIBE AMENE
AMABWERA
KUDZABADWANSO.

PAMENE MTEMBO WA MUNTHU WA CHUMA UJA UMACHOKA KUMUNDA KWAKE KUPITA KUMANDA, ANTHU ANAONA KUTI NAYENSO LAZARO WOPEMPHA UJA WAMWALIRA.

A man in a blue and gold robe is kneeling on the ground, looking down at a man lying on his back. The man on the ground is wearing a red robe and has a long white beard. The background shows a stone wall and a tree.

NDI **LAZARO**,
MKULU WOPEMPHA UJA.
NAYENSO WAMWALIRA
USIKU WATHAWU. KOMA
AKUONEKA KUTI WAFWA
MU MTENDERE.

THUPI LA LAZARO
ANALINYAMULIRA PA NGOLO
KUPITA NALO KUMALO KUMENE
NYAMA ZAKUFA AMAZITAIRA,
NKUZIOTCHA. SANACHITE
MWAMBO WA MALIRO NDIPO
PALIBE AMENE ANAMULIRA.




KOMA ANGELO
ANABWERA NANYAMULA
LAZARO KUPITA NAYE
KU PARADIZO.

EEE! ULENDU WABWINO
BWANJI! SINDINKAGANIZA
KUTI KUMWALIRA KUNGAKHALE
KOSANGALATSA CHONCHI!

LAZARO, MBALE
WATHU, TAKULANDIRA.
SUDZAMVANSO NJALA NDIPO
THUPI LAKO SILIDZAWAWA.
BWERA, TAKUKONZERA
CHAKUDYA.

MUNTHU WACHUMA UJA ANAMUIKA MWAPAMWAMBA ZEDI
M'MANDA ABWINO KWAMBIRI, NDIPO ALIYENSE AMENE
ANKAKONDA NDALAMA ZAKE ANABWERA KUDZAONA
CHIMENE ANAWASIYIRA M'CHIKALATA CHONENA ZA
KAGAWIDWE KA KATUNDU.





ANALI MUNTHU
WABWINO. INDE NTHAWI
ZINA ANKAONEKA NGATI WOLIMA
MTIMA KWA AMENE ANKAWAKONDA,
KOMA TIDZAMKUMBUKIRA NTHAWI
ZONSE KUTI ANKAKONDA DZIKO
LAKE NDIPONSO KUTI ANALI
WACHILINGAMO M'ZOCHITA
ZAKE.

WAPITA
KUKALANDIRA
MPHOTHU YAKE.
MZIMU WAKE UWUSE
MU MTENDERE
WOSATHA.

KOMA PAMENE MUNTHU
WACHUMAYO
ANAMWALIRA ANAPEZEKA
KUTI ALI M'DZENJE
LAKUYA KWAMBIRI.



LUKA 16:22




**THANDIZENI!
INU MULUNGU,
THANDIZENI! NDILI
KUNO NDIPO NDILI
KUPSA NDI MOTO!**

TATE WANGA **ABRAHAMU**,
MUNDICHITIRE CHIFUNDO. NDIKUONA
LAZARO KUMENEXO. MUUZENI KUTI ATENGE
MADZI KU CHALA CHAKE NDIPO ADZAZIZIRITSE
LILIME LANGA, POPEZA NDIKUVUTIKA
KWAMBIRI NDI MOTO.



NDIPOTU MUMTUMIZE
LAZARO KU NYUMBA YA BAMBO
WANGA KUTI AKACHENJEZE ABALE
ANGA KUTI ASADZAONE ZIMENE
NDIKUONA INEZI M'MALO
OZUNZA ANO.





MWANA WANGA,
NKADAKUTHANDIZA NDITHU NKADAFUNA,
KOMA PALI PHOMPHO LALIKULU PAKATI
PATHU, NDIPO PANSI PAKEPA PALI NYANJA
YA MOTO. SITINGAOLOKE KUDZAKUTHANDIZA,
NDIPO IWENSO SUNGAOLOKE KUBWERA
TSIDYA LINO.




ALI NDI
ZIMENE MOSE NDI
ANENERI ADALEMBA.
ANGOKHULLUPIRIRA MAU
A MULLINGU.

LUKA 16:22-31



KOMA ZIMENEZI
SIZINGAWAKWANIRE. ATAONA
CHOZIZWITSA CHOTI WINA WALIKA
KWA AKUFA, AKHOZA KULAPA TCHIMO
LAO LA KUSAKHULLUPIRIRA.

NGATI SAKHULLUPIRIRA
MAU A MULLINGU, SANGATEKESEKE
NGAKHALE ATAONA KUTI WINA WALIKA
KUMANDA. WACHEDWA NAZO.
ADZISANKHIRE OKHA. PEPA. PALIBE
CHIMENE NDIINGACHITE.



EYI, ANYAMATA
INU. KODI MUFUNA
KUSANGALALA?
NGATI MUKUNDIFUNA
NDINE PANO, INE
SINDIVUTA.

AMBUYE, MLEKENI
AMENEYU. ANTHU ONGA
IYEYU MPOVUTA KUTI
ATEMBENUKE MTIMA
CHIFUKWA ADAKHAZIKIKA
M'ZOIPA ZAOZO.



MAU A MULLINGU AMATI,
"USACHITE CHIGOLOLO."

EYI, INETU
NDINE MAI
WOPEMBEDZA.
NDIMAKHULLUPI
RIRA
MULLINGU.

SATANA WAKUNYENGA.
PALIBE KUCHITIRA MWINA
KOMA UZATHERA
M'NYANJA YA MOTO.



MUNAMVA MOMWE
ANANENERA ANZANU. MPOVUTA
KUTI ANTHU NGATI INE
ATEMBENUKE MTIMA. NDAKHALA
NDIKUCHITA CHIWEREWERE NDI
AMUNA OSIYANASIYANA
KUYAMBIRA LIBWANA WANGA.



PALIBE CHOSATHEKA
NDI MULLINGU. UKAMUFUNA,
LIDZAMUPEZA. ADZAKUKHULLUKIRA
MACHIMO AKO NDIPO
ADZAKONZANSO MOYO WAKO.

MOYO WANGA NDI
WA SATANA KOMA NDIKHOZA
KUUPEREKA KWA MULLINGU NGATI
ATAFUNA...ATAFUNA...ATAFUNA...
ATAFUNA...ATA...ATA...



EEEEAAIIIIII!



**ALI NDI
ZIWANDA
ZAMBIRI!**

FUTUKANI!

**EKSODO 20:14; LUKA
8:2; 1 YOHANE 1:9**



EEEEII!

**SATANA,
TULUKA MWA
IYE!**



NDIKUKULAMULA
KUTI UTULUKE NDIPO
USADZABWERENSO
MWA IYEYU.


YESU ATALAMULA,
ZIWANDA ZISANU NDI
ZIWIRI ZINATULUKA
MWA MKAZIYO.



ZAPITA!

**NDINU
YANI?**

**NDINE
YESU.**




USIYE MACHIMO AKO
NDIPO UZIPEMBEDZA MULLINGU,
KOMA UKAPANDA KUTERO ZIWANDA
ZIJA ZIDZABWERANSO MWA IWE NDIPO
ZIDZABWERETSANSO ZINA ZOIPA
KWAMBIRI KUPOSA IZOZO.

CHAMUCHITIK
IRA
NCHIYANI?

NDIFUNA
KUTUMIKIRA
MULLINGU.
NDIDZAKUTSATANI
KUTI NDIPHUNZIRE
ZAMBIRI.


DZINA LA MKAZIYO LINALI
MARIYA WA KU MAGADALA.



AMBUYE, NDINAONA
CHIMENE CHINKACHITIKA.
NCHODABWITSA NDITHU.
ATSOGOLERI ATHU ACHIPEMBEDZO
ANKATHA KUMUSASA MARIYA WA KU
MAGADALA MASANA, KOMA ENA
ANKAPITA KUNYUMBA KWAKE
USIKU. MWAMUPATSA
MOYO WATSOPANO.


TIBWERA.

NDIKUPEMPHANI
KUTI INU PAMODZI
NDI OPHUNZIRA ANU
MUBWERE KUNYUMBA
KWANGA KUTI MUDZADYE
CHAKUDYA. NDIKUFUNA
KUTI ANZANGA ENA
AKAMVE ZAMBIRI
KWA INU.




YESU, TIUZENI,
KODI MUNTHU
ANGATHE BWANJI
KUKHALA
WACHILUNGAMO NDI
WOYERA MTIMA
M'DZIKO LAZIPHUPHULI?
TITAPANDA KUPINDA
LAMULO PANG'ONO,
TIKHOZA KUFA NDI
NJALA.

MUSAMAVUTIKE NDI ZINTHU
ZOTI ZIMATHA, KOMA NDI
ZIMENE ZIMAKHALA MPAKA
MUYAYA. MUSAMAGANIZIRA
ZA CHUMA CHANU CHOKHA,
KOMA MUZIGANIZIRA MMENE
MUNGAKHALIRE DALITSO
KWA ANZANU.



MOYO UMAPOSA
CHAKUDYA NDI
ZOVALA. NGATI
MULLINGU AMAVEKA
MALLIWA A KU TCHIRE,
ADZAKUVEKANI
INUNSO.


IKUDZA NTHAWI
PAMENE MULLINGU
ADZAWERUZA MUNTHU
ALYENSE, NDIPO MUNTHU
ALYENSE ADZAYANKHA
ZIMENE ADACHITA;
ZABWINO KAPENA
ZOIPA.



MUSAMAKHALE NGATI
ATSOGOLERI ACHIPEMBEDZOWA,
PAKUTI AMALALIKA ZINA, NKUMACHITA
ZINA. ALI NGATI ZIKHO ZIMENE
ZIMAONEKA ZOYERA KUNJA KOMA
M'KATI MULI MOIPA.

NGATI
KULLUNGAMA KWANU
SIKUPOSA IWOWA,
SIMUDZALOWA MU
LIFUMU WA
MULLINGU.

MLALIKI 12:14; MATEYU 23:25, 6:19-21, 25,
28-30, 12:36; LUKA 15:1-3




CHONCHO, LIMALANDIRA
OCHIMWA, NKUMAKHALA NAWO
MPAKA KUMADYA NAWO PAMODZI.
NDAONA KUTI MARIYA WA KU MAGADALA
ALI POMPARO PAMODZI NDI OCHIMWA
AWA. UNGANENE BWANJI KUTI NDIWE
WOYERA PAMENE UKUDYA NDI
ANTHU OTERE?

NDIKULUZANI
NTHANO IMENE
IMAKAMBA ZA
CHIKONDI CHA
MULUNGU.



MUNTHU WINA
ADAALI NDI ANA
AAMUNA AWIRI. MWANA
WACHIWIRI ANALI
WOSAMVERA NDIPO
ANAFUNA KUKHALA
MOYO WOMACHITA
ZOMWE AKUFUNA.

EEE,
NDIMA KON
DA NTHANO
IMENEYI.




CHONCHO
ANAFUNA KUTI
ALANDIRIRETU
CHOLWA
CHAKE.

ABAMBO,
MUKANDIPATSA
MBALI IMODZI YA
MUNDA WANU NGATI
CHOLWA CHANGA,
NDIPITA MU MZINDA
KUKACHITA ZIMENE
ZINGANDIPINDULIRE.



KOMA MWANA WANGA,
ZONSE ZIMENE NDILI NAZO NDI
ZAKO. INETU NDIFA POSACHEDWAPA
NDIPO IWE NDI MKULLU WAKO MUDZATENGA
ZONSEZI KUTI ZIKHALE ZANU. MUDZAKHALA
PABWINO MOYO WANU WONSE. TILI NDI
NKHOSA NDI NG'OMBE ZAMBIRI. NDIPO
TIMAKOLOLA ZOCHULUKA CHAKA NDI
CHAKA CHIFUKWA MINDA YATHU NDI
YACHONDE. TILI NDI ANTCHITO
AMBIRIMBIRI NDIPONSO...

KOMA NDIKUFUNA KUTI
NDICHOKE NDITHU KUTI NDIKAONE
MMENE DZIKO LILILI. SINDIKUFUNA
KUKHALA PAMUNDA PANO MOYO
WANGA WONSE NDI KUMAGWIRA
NTCHITO NGATI KAPOLO. NDILI
MNYAMATA CHONCHI NDIFUNA
NDISANGALALEPO. ANZANGA...




ANZAKO, AMENE SAGWIRA
NTCHITO, AMANGOGANIZA
ZOTI KODI HATCHI YOTHAMANGA
KWAMBIRI NDI ITI, VINYO
WABWINO KWAMBIRI NDI UTI,
NANGA AKAZI OSANGALATSA
KWAMBIRI NDI ATI.

KODI MUMADZIWA MMENE MOYO
UMAKHALIRA? MUMANGOKHALA PHWII PA
MUNDA WAKALEKALEWU. NDIKUFUNA
MUNDIGAWIRIRETU MBALI INA YA MUNDA
WANUWU TSOPANO LINO. NDIKUPITA KU
MZINDA KOMWE NDIZIKAKHALA MONGA
MOMWE NDIFUNIRA POPANDA WINA
WONDISOKONEZA.

MPATSENI. TIDZAKHALA
BWINOBWINO POPANDA
IYEYU. PAJATU NTHAWI ZONSE
SAGWIRA NTCHITO YOMWE
WAPATSIDWA.





BAMBO UJA
ADAMPATSA MWANA
WAKEYO CHUMA CHIMENE
ANKAFUNACHO. CHONCHO
MWANAYO ANACHOKA, NAOLOKA
NYANJA, KUPITA KU MIZINDA
IKULUIKULU KUMENE ANKATI
AKAPEZAKO CHISANGALALO.

TSOPANO UKU
NDIKO KUKHALA -
PALIBE WINA
WONDIUZA
ZOCHITA.


LUKA 15:11-13



MWANA
WAMNG'ONO...


EYAA, IZI
NZABWINO KUPOSA
MMENE NDINKAGANIZIRA.
TAONANI ANTHU ONSEWA
NDIPONSO NYUMBA.
KUNO NDIYE KUCHIMAKE
KWA CHISANGALALO.

NDIYENERA
KUPEZA MALO
OGONA ABWINO
KWAMBIRI OMWE
NDIZILIPIRA.




EYAA, IYI
IKUONEKA YABWINO
KOPOSA. NDIZIKHALA
M'MENEMU.

NGATI MUFUNA
TIKUTHANDIZENI
MUNGOTIFUNSA.
TIMATUMIKIRA USANA
NDI USIKU WOMWE.

A man with a beard, wearing a blue tunic and a purple blanket, is lying in a bed. He is looking towards the right. The room is decorated with classical elements: a bust of a woman on a pedestal, a vase of flowers on a table, and a full-length statue of a man on a pedestal. The background features a window with a lattice pattern and a doorway.

NDANINSO AMENE
ANGAFUNE MALO ENA
OPOSA AWA? MAWA
NDIPITA KUKAKUMANA NDI
ANTHU ENA
MUMZINDAMU.

LUKA 15:13



EEI, NDANI UYU?
MNYAMATA
WACHIMIDZIMIDZI.
TITAONA NKHOPE YAKE,
ANGAONEKE KUTI
NGOKONGOLA.

EEI, MNYAMATA,
NGATI UKUFUNA KUTI
USANGALALE NAFE, NDI
BWINO KUTI LIMETE
KAYE NDEVU ZAKOZI
NDIPONSO LIPEZE
ZOVALA ZABWINO OSATI
ZIMENE WAVALAZI.

TADZIONA.
UKUONEKA BWIN
NDI ZOVALA
ZATSOPANOZI.






TAKONDWA KUTI
ULI NAFE PAMODZI
PA CHAKUDYA
CHAMADZULOCHI.

AKUONEKATU
BWINO TSOPANO
CHIFUKWA WACHOTSA
NDEVU ZIJA.
SICHONCHO?



TILANDIRE
MNZATHU WATSOPANOYU.
NTHAWI ZONSE AZIPEZA
CHISANGALALO NDI
CHIMWEMWE.

...NDI
CHIKONDI.



MNYAMATA,
BWERETSA
VINYO WINANSO
KUTI ANZANGA
AMWE.

LUKA 15:13


KODI SITINGAPITE
KUMENE UMAKHALA,
IWEYO NDI INE?



CHONCHO MNYAMATA
UJA, KUTALI NDI KWAO,
ANAKHALA ALI NDI NDALAMA KWA
MIYEZI YAMBIRI NDITHU. PAMENE
ADALI NDI NDALAMA, ANALINSO
NDI ABWENZI AMBIRI.



TSIKU LINAFIKA PAMENE
CHISANGALALO CHAKECHO
CHIDAMUTHERA NDALAMA
ZONSE - KOMA ADALI NDI
ABWENZI AMBIRI AMENE
ANALI OLEMERA KWAMBIRI.



UKAMATI ULIBE
NDALAMA
UKUTANTHAUZA
CHIYANI? KODI
SUJA UDAALI
WOLEMERA?


ZOONADI, KOMA KUKHALA
KUNO PAMAFUNIKA NDALAMA
ZAMBIRI, NDIPO NDALAMA
ZIMENE ZIDANDITSALIRAPO
NDINATHERA NJUGA SABATA
LATHA. NDIMAGANIZA KUTI
NDIPAMBANA NJUGAYO,
KOMA...

UKUTANTHAUZA CHIYANI
UKATI ULIBE CHILICHONSE?
NANGA DERESI LIJA
UDANDILONJEZA
UNDIGULIRA BWANJI?

NDIMAYEMBEKEZA
KUTI ABAMBO AKO
ANDILEMBA NTCHITO
YOSAMALIRA
CHUMA CHAO?

NTCHITO?





SINDIKUKHULUPIRIR
A KUTI
NDIKUDYETSADI
NKHUMBA - NYAMA
ZODETSEDWA,
ZALVE.

NDIMAGANIZA KUTI
NDILI NDI ABWENZI.
SANDIYANKHULITSANSO
TSOPANO. KOMA
NDIPEZA NTCHITO INA
NDIPO
NDIDZALEMERANSO.

MHU


MHU

MHU


SINDILABADAKO ZA MMENE
WADWALIRA. DZUKA PAMENEPO
KUTI UKASAMALE NKHUMBA.
NDIKUCHOTSA NTCHITO NDIPO
NDILEMBA WINA. NYAMUKA
TSOPANO LINO!



INDE,
BWANA, PEPANI.
NDIKUPITA
POMPANO,
BWANA.



NDALAMA ZIMENE
NDIMALANDIRA POGWIRA
NTCHITOYI NDI ZOCHÉPA
KWAMBIRI NDIPO SINDIDYA
BWINO. NDIGANIZA KUTI
ANZANGA AJA
NDINKASANGALALA NAWO
AKUDYA BWINO.



ONANI MOMWE NDILILI
TSOPANO. NDIKUMVA KUZIZIRA,
NDILI NDI NJALA, KOMANSO
NDATOPA. NDIKHOZA KUDYA CHAKUDYA
CHANKHUMBACHI. ANTCHITO A ABAMBO
ANGA ALI NDI CHAKUDYA CHOCHULUKA
KWAMBIRI NDIPO AMADYA MOMWE
ANGATHERE. NDIKADAPITA...KOMA IYAYI,
SINDIKUFUNA NDITABWERERA,
SINDIDACHOKE BWINO. AKHOZA
KUKANDINYOZA.


NDASANDUKA WOPLISA
KWAMBIRI. NANGA NDITABWERERA
NDIKUKAWAPEMPHA KUTI NDIKHALE WANTCHITO
WAO? NDIDAMALIZA CHOLOWA CHANGA
CHONSE. KOMA NDIKHOZA KUKAKHALA
WANTCHITO - AKAKANDILANDIRA.





NDIKUPITA
KWATHU.

WOPUSA IWE!
ULIBE NDALAMA.
UYENERA KUYENDA
MTUNDA WAUTALITALI
KUTI UKAFIKE
KWANUKO.



ATAYENDA KWA
MILINGU INGAPO,
ANAYANDIKIRA
KWAO.

NDAKHALA PANG'ONO
KUFIKA. NDILIBE MPHAMVU
ZOKAPEMPHERA KUTI ANDICHITIRE
CHIFUNDO. NDIKANENA KUTI, "ATATE,
NDAKUCHIMWIRANI NDIPO
SINDIYENERANSO KUTCHEDWA
MWANA WANU. MUZINDIONA INE
NGATI MMODZI MWA
ANTCHITO ANU."

LUKA 15:16-19

MUKUMUONA MUNTHU AMENE
AKUBWERA APOYO? MASO ANGAWA
ADAKALAMBA NDIPO SAONA MONGA
KALE, KOMA AKUYENDA NGATI MWANA
WANGA AMENE ADALOWERERA
KALEKALE.



INDE, NDI
WOKULIRAPO,
NDIPONSO
WOWONDA, KOMA
NDIKUKHULLUPIRIRA
KUTI NDI MWANA
WANU.




**MWANA
WANGA!**



MWANA WANGA,
MWANA WANGA,
WAFIKA KWANU!

ATATE,
NDAKUCHIMWIRANI...




...NDIPO
SINDIYENERA
KUTCHEDWANSO
MWANA WANU.

TIMAYESA KUTI
UDAMWALIRA, KOMA
UKADALI NDI
MOYO. TIYENERA
KUKUSAMALA
POMPANOPOMPANO.


SUNGAPITE KU NYUMBA
MMENE UKUONEKERAMU. WANTCHITO
WANGA ABWERETSA CHOVALA CHABWINO
NDI NSAPATO ZOTI LIVALE KUPHAZI
KWAKOKU. MPHETE YAKO IJA IDASOWA.
INDE, UYENERA KUKHALA NDI MPHETE.
MWANA WANGA AMENE ADATAYIKA
TSOPANO WAPEZEKA.



IPHANI
MWANAWANG'OMBE
WONENEPWA BWINO,
KONZANI PHWANDO,
ITANANI ANTHU, KUTI
TISANGALALE, PAKUTI
LERO NDI TSIKU LOTI
TIKONDWERE.




NDAKONDWA KUTI
NONSENU MULI PANO
KUDZASANGALALA NDI INE PA
CHIKONDWERERO CHINO. MWANA
WANGA AKADALI WOFOOKA CHIFUKWA
CHA ZIMENE WADUTSAMO, KOMA
CHIFUKWA CHA CHAKUDYA CHABWINO
AKHALANSO WAMPHAMVU
POSACHEDWAPA. LERO NDI
TSIKU LOPAMBANA PA
MOYO WANGA.



MWANA WAMKULLU
ADAACHOKAPO KWA MASIKU
AMBIRI NDITHU. ATABWERERA
KU MUDZI, ANAPEZA
PHWANDO LILI M'KATI.

NANGA NYIMBOZI
NDIPONSO KUVINA
KUMENE NDIKUMVA?

MNG'ONO WANU
WABWERERA KWAO KUNO ALI
WOMVETSA CHISONI. AKUDWALA
NDIPONSO NDI WOSAIKA. ATATE
ANU AKUKONDWERERA CHIFUKWA
CHOTI MNG'ONO WANLIYO
WABWERA. FULLUMIRANI
KULOWA M'KATIMO.



SINDINGACHITE
NAWO ZOPUSAZO.
IYEYU WAKHALA
M'MOYO WOCHIMWA
NDI WOCHITITSA
MANYAZI.

WANTCHITO UJA ANAKAUZA
ATATEWO ZOMWE MWANA
WAO WAMKULU ADANENA,
NDIPO ANATULLIKA
KUDZAYANKHULA NDI
MWANA WAKEYO.

KWA NTHAWI YAITALI
NDAKHALA NDIKUMUFUNAFUNA,
NDIMAYESA KUTI ADATAYIKIRATU.
NDIDAKHALA PANG'ONO KULEKA
KUMFUNAFUNA KOMA PANO WABWERA.
LINGALIMVETSE DALITSO LIMENELI?
MULLINGU NDI WABWINO!



SINDIKUMVETSA
CHIFUKWA CHOMWE
MUKUKONDWERA NDI MUNTHU
WOCHIMWAYO. INE
SINDIKONDWERA NAWO
ZIMENEZI.



NTHANO IMENEYI NDI
YOSANGALATSA. KOMA KODI
UKUGANIZA KUTI IFE TILI NGATI
MWANA WAMKULU UJA?

AMENE ALI NDI
MAKUTU, AMVE.

LUKA 15:23-32



MUNTHU UYU
NDI WOOPSA. ANTHU
ONSE AKUMUKONDA.

AMAWAPATSA
CHIYEMBEKEZO.


INDE, KOMA CHIYEMBEKEZO
CHAKE NDI CHABODZA. NDANI AMENE
ANGALONJEZE MOYO WOSATHA KWA
MUNTHU WOCHIMWA? AYENERA KUFA
BASI. MUITANE ANTHU ENA. TIKUMANA
USIKU UNO KUNYUMBA KWA
MKULU WA ANSEMBE.

TIYENI TIPITE KU GALILEYA KUTI
TIKAPUMULEKO PANG'ONO. NTHAWI IKWANA
POSACHEDWAPA PAMENE ADZANDIPONYA
M'NDENDE. ADZANDINYOZA NDIPO PAMBLIYO
PAKE ADZANDIPACHIKA PA MTANDA. KOMA PA
TSIKU LACHITATU NDIDZAUKA KUMANDA.

AKUTANTHAUZA
CHIYANI PONENA
KUTI, 'ADZAUKA
KUMANDA?'

SINDIKUDZIWA.
MWINA NDI
NTHANO.






AMBUYE, ZADZIDZIDZI!
MARITA WANDITUMA KWA
INUYO. LAZARO, MLONGO WAKE,
WADWALA KWAMBIRI MOTI SIZILI
BWINO. LAZARO NDI MNZANU
WAPAMTIMA. MUKAFULUMUIRA
MUKAFIKA ASANAFE.
TIKUDZIWA KUTI MUKHOZA
KUMUCHIRITSA.

MUDZIWITSE MARIYA
NDI MARITA KUTI NDIKUBWERA.
MUWALIZE KUTI CHOLINGA CHA
KUDWALAKO SI IMFA, KOMA KUTI
MULUNGU ALEMEKEZEKE.


LAZARO
WADWALA?
TIYENERA
KUFULUMIRA!

**PATAPITA
MASIKU AWIRI**



**AMBUYE, PAPITA
MASIKU AWIRI TSOPANO
KUCHOKERA PAJA TIDAMVA
ZOTI LAZARO AKUDWALA
MODE TSA NKHAWA, NDIPO
KUTI TIKAFIKE KUMENEKO
PAPITANSO MASIKU ENA
AWIRI. KODI TIKHOZA
KUYAMBAPO?**

**TINYAMLIKA
MAWA.
MUDZAONA
ULEMERERO WA
MULINGU.**



AMBUYE, MASIKU
OPOSA ANAI APITAPO.
KODI TIKAFIKA PA NTHAWI
YAKE KUTI WODWALAYO
ATHANDIZIKE?

LAZARO WAMWALIRA. NDIPO
NDAKONDWA, CHIFUKWA CHA
INU, KUTI WAFWA INE KULIBE,
PAKUTI TSOPANO MUDZAONA
ULEMERERO WA MULLINGU
NDIPO MUDZAKHULLUPIRIRA.

**WAMWALIRA?
LAZARO
WAMWALIRA?**

MATEYU 20:17-20; YOHANE 11:11-15




YESU NDI
OPHUNZIRA AKE
ALI KUNJA KWA
CHIPATA.

AAAAAAA!

MAYOOO!

MUWALIZE KUTI ANDIDIKIRE
POMWEPO. SI BWINO KUTI AFIKE
AFARISI NDI ANSEMBE ONSEWA
AKUONA. AKUFUNABE KUMUPHA.

**IWE
LAZARO!**



AMBUYE, MUKADAKHALAPO
MLONGO WANGA SAKADAMWALIRA.
KOMA NGAKHALE TSOPANO
MUKHOZA KUPEMPHA CHOMWE
MUFUNA NDIPO MULINGU
ADZAKUCHITIRANI CHIMENECHO.


MLONGO
WANU ADZAIKA
KUMANDA.

NDIKUDZIWA
KUTI ADZAIKA PA
NTHAWI YA
CHIUKITSO, PAKUTHA
PA DZIKO.



INE NDINE
KUKA NDI
MOYO.

YENSE AMENE
AMAKHULLUPIRIRA INE,
NGAKHALE AMWALIRE,
ADZAKHALANSO NDI MOYO.
NDIPO ANTHU AMOYO
AMENE AMAKHULLUPIRIRA
INE SADZAMWALIRA
KONSE. UKUKHULLUPIRIRA
ZIMENEZI?

A close-up comic book illustration of a woman with a blue headscarf. She has a surprised or earnest expression, looking upwards and to the right. Her mouth is slightly open as if speaking. Her right hand is raised, with fingers spread, in a gesture of emphasis or explanation. The background is a simple blue gradient.

**INDE, AMBLIYE.
NDIMAKHULLUPIRIRA
KUTI NDINU MESIYA,
MWANA WA MULLUNGU,
NDIPO ZA KUBWERA
KWANU M'DZIKO LAPANSI
ZIDANENEDWA KALE
NDI ANENERI.**

ATAYANKHULA NDI
YESU, MARITA
ANATUMA WANTCHITO
KUTI AKAITANE MARIYA.

BWERANI.
AKUPITA KU
MANDA
KUKAKHUZA.

OOOOOO

YOHANE 11:17-31





AMBUYE,
MUKADAKHALA
KUNO, MLONGO
WANGA
SAKADAMWALIRA

MWAMLIKA
KUTI?



TAMUSOWA
KWAMBIRI.



ONANI MOMWE
YESU
ANKAMUKONDERA.

KODI IYE AMENE
WAPENYETSA
MUNTHU WAKHUNGU
SAKADACHITITSANSO
KUTI BWENZI LAKE
ASAMWALIRE?




**CHOTSANI
MWALAWO.**

**KODI
SINDIDAKUZENI
KU MUKANDIKHULUPIRIRA
MUDZAONA ULEMERERO
WA MULLINGU?
TANGOCHOTSANI
MWALAWO.**

**KOMA AMBLIYE,
PANOPA
AKUNUNKHA, POPEZA
PADUTSA MASIKU
ANAYI
CHIMWALIRENI.**

ATATE, NDIKUYAMIKANI
CHIFUKWA MUMANDIMVERA.
SINDIKUPEMPHERA ZIMENEZI
CHIFUKWA CHA INE MWINI,
CHIFUKWA NDIMADZIWA KUTI
NTHAWI ZONSE
MUMANDIKONDA, KOMA
NDIKUPEMPHERA KUTI AMENE
AKUONA IZI AKHULUPIRIRE KUTI
MUDANDITUMA. TSOPANO
ATATE DZILEMEKEZENI
NOKHA.



YOHANE 11:32-42



**LAZARO,
TULLUKA.**

**WANYANYA
TSOPANO.**

**INDE,
AKUDZIPUSIT
SA YEKHA.**



THUPITU
LIDAONONGEKA
KALE.

ANTHU AKAONA
OKHA KUTI IYEYU NDI
WABODZA, SIKUKHALA
KOVUTA KUMUGWIRA
NDI KUMUPHA.



**CHIYANI?
SINDIKUKHULU
PIRIRA ZOMWE
ZACHITIKAZO!**

SIZOONA!



**ULEMERERO
UKHALE KWA
MULUNGU!**

OHOOOOOO!



**WACHITADI,
MARIYA!
WACHITADI!**

**ALI NDI MOYO!
PATATHA MASIKU
ANAI, ALI NDI
MOYO TSOPANO.**

YOHANE 11:43-44

LAZARO, PATAPITA MASIKU
ANAI CHIMWALIRIRENI,
ANAIKA KUMANDA, MANJA
NDI MIYENDO YAKE ZILI
ZOMANGIDWA NDI NSALU
ZOIKIRA MALIRO.

MMASULENI
AZIPITA!



NDANI AMENE
ANGACHITE
ZOTEREZI KOMA
MULLINGU?



BWANJI KODI?
MASULENI NSALU
ZOIKIRA MALIROZI.

PADUTSA
MASIKU ANAI ULI
CHIMWALIRIRE.

AMBUYE, NDAKONDWA
KUTI NDAKUONANI.
NDIKHULLUPIRIRA KUTI
NDINU AMENE
MWANDIPATSANSO
MOYO.



LAZARO,
TINAKUSOWAT
U KWAMBIRI.

NDIKUMVA NJALA.
OLIRAWA AUZENI KUTI
AZIPITA KWAO KUTI
IFE TIDYE.


WODALITSIKA
NDINU, AMBLIYE
MULUNGU WATHU.

LINGAZIKHULUPIRIRE ZIMENE
TAONAZI? SIKUTI WATIPUSITSA AI.
NDIDAMUONA LAZARO ASANAMUIKE
M'MANDA. ANALIDI WAKUFA.



ANTHU A KU
YERUSALEMU AKAMVA
ZIMENEZI, AMULONGA
UFUMU. TIYENERA
KUCHITAPO KANTHU
MSANGAMSANGA.

TIWALIZE
MSANGA ALEMBI
A MALAMULO
NDI AFARISI.




YESU UJA
WAPUSITSA ANTHU
KWAMBIRI LERO.
KOMA ANTHU AMENE
ANAONA ZIMENEZO
AKUGANIZA KUTI
ANALITSADI MUNTHU
KUMANDA.

KAYA ANACHITA
BWANJI ZIMENEZI,
IFE SIZIKUTIKHUDZA;
NGATI SITIMULETSA,
AKOPA ANTHU
ONSE.


PAKAONEKA KUTI
TALKIRANSO, AROMA
ATILANDA MPHAMVU
ZOLAMULIRA. AMAFUNA
KUTI TIZISUNGITSA
MTENDERE.

YOHANE 11:44-28



KOMA YESU
SANACHITEPO
ZACHIWAWA KAPENA
KUNYOZA AROMA.

MAU AKE NGODZETSA
CHIWAWA! AMATINENA PAGULU
KUTI NDIFE ACHINYENGO.
ANTHU AMATISEKA. ANTHUTU
AMATINYOGODOLA
POYERAYERA.



AYENERA
KUCHOTSEDWA.
SADZATHA
KUDZIUKITSA
KUMANDA.

TICHITE
POSACHEDWAPA,
ASANATIONONGERE
ULEMU CHIFUKWA
CHA CHIPEMBEDZO
CHATHU.


AROMA
ASANATITEMBE
NUKIRE.

ANDIKANA NDIPO AFUNA
KUNDIPHA. SAKUDZIWA KUTI INE
NDINABWERA KUTI NDIWAPULUMUTSE.
NDIKUKUUZANI KUTI INE NDIKADZAPITA,
AROMA ADZABWERA KUDZAONONGA
NYUMBA YA MULUNGU IMENE AYUDA
AMA KONDA. IDZAONONGEKERATU,
KOTERO KUTI PALIBE MWALA UMENE
UDZAKHALE UTASANJIKIZANA
NDI UNZAKE.




NTHAWI IDZAFIKA PAMENE ONSE
AMENE AMANDIKONDA ADZAPONYEDWA
M'NDENDE. ANTHU ONSE ADZADANA
NANU CHIFUKWA CHOTI
MUMANDIKONDA. ENANU MUDZAFERA
M'MANJA MWAO. ENA ADZAWATULUTSA
M'NYUMBA ZAO NDIPO SADZAWALOLA
KUMAGWIRA NTCHITO.






MUKADZAONA ZINTHU IZI
ZIKUCHITIKA MUSADZADABWE,
PAKUTI PADZAONEKA NKHONDOZAMBIRI,
ZIVOMEZI, MATENDA, NJALA,
NDIPONSO ZOWAWA
ZAMITUNDUMITUNDU, KOMA
CHIMALIZIRO SICHIDZAFIKA CHIFUKWA
CHA ZINTHU ZIMENEZI.




ZIMENEZI NDI CHIYAMBI
CHABE CHA MAZUNZO. MU
YERUSALEMU MUDZAKHALA ANTHU
A MITUNDU INA KUFIKIRA
ITAKWANIRITSIDWA NTHAWI IMENE
ANTHU A MITUNDU INAWO AYENERA
KUKHALA M'YERUSALEMUMO. WINA
AKADZAKULUZANI KUTI INE NDABWERA
NDIPO KUTI INU MUPITE UKU NDI
UKO, MUSADZAKHULUPIRIRE
ZIMENEZO. AMBIRI ADZABWERA
NKUMANAMIZA ANTHU KUTI NDINEYO
KAPENA KUMAYANKHULA
MONAMA M'MALO MWANGA.



KOMA INE NDIKAMADZABWERA,
NDIDZABWERA NGATI CHIPHALIWALI. DISO
LILILONSE LIDZANDIONA. ANTHU AKUFA ADZALUKA
NDIPO NDIDZAKHAZIKITSA UFUMU WANGA PA
DZIKO LAPANSI. KOMA IZI ZISANACHITIKE,
PADZAFIKA KAYE NTHAWI YA MASALUSO AAKULU
KWAMBIRI, KUPAMBANA ZONSE ZIMENE DZIKO
LAPANSI LIMATI NZOSALUSO.

MATEYU 10:22, 24:2, 5-9, 27-31; LUKA 19:43-44,
21:8; YOHANE 11:49-53; CHIVUMBULUSO 2:10



AMBUYE, MARITA
WANDITUMA KWA INU.
AKUTI NDIKUUZENI KUTI
INUYO NDI OPHUNZIRA ANU
MUBAKAKHALA KWAO. KU
YERUSALEMU SIKULI BWINO;
AKAKUCHITANI CHIPONGWE.
ANTHU NDI OKHUMUDWA
CHIFUKWA CHOTI MUDADZUTSA
ABWANA ANGA KUMANDA.
KODI SIMUNGABWERE KUTI
MUBADZAKHALA NAFE?


TAKONDWA NDIPO
TIBWERADI. NDIMAFUNA
NDITAWAONANSO NTHAWI
YANGA YA MAYESERO
ISANAFIKE.



NDI YESU NDI
OPHUNZIRA AKE.

AMBUYE, NYUMBA
YANGA NDI YANUNSO.
CHONDE LOWANI KUTI
MUPUMULE.

LAZARO, MNZANGA,
UKUONEKA BWINO KUSIYANA
NDI NTHAWI IJA NDIDAKUONA.
NDI BWINO KUTI NDIBWERE
KUNYUMBA KWAKO OSATI
KUMANDA KWAKO.



TAKONZA
PHWANDO. TAITANA
ALENDO.


AMBUYE, INU
NDINU KUUKA
NDI MOYO.

MATEYU 20:19, 26:2; YOHANE 12:1-2, 14:6



AMBUYE, NDAMVA
NDITHU KUTI AYUDA
ATSIMIKIZA ZOKUGWIRANI
NDI KUKUPHANI.

NDINABWERA M'DZIKO LAPANSI
KUTI NDIDZAPEREREKE MOYO WANGA KU
DZIKO LAPANSILO. NDIDZAPONYEDWA
M'NDENDE NDIPO NDIDZAKHOMEDWA
PA MTANDA, KOMA PA TSIKU
LACHITATU NDIDZALKANSO.




INU NDINU
KULIKA NDI MOYO,
AMENE AMAKHULLUPIRIRA
INUYO SADZAMWALIRA
KONSE.

MARIYA,
UKUCHITA CHIYANI
NDI MAFUTA
OSUNGIRA MALIRO
KUTI ASAOLE?





MBUYE WANGA,
INU NDINU KUUKA
NDI MOYO. NGAKHALE
MUPHEDWE,
MUDZAKHALANSO
NDI MOYO.



MARIYA, MTENGO WA
MAFUTA AMENEWU NDI
MALIPIRO A CHAKA CHONSE
A MUNTHU WAGANYU.
NCHIFUKWA CHIYANI
UKUWAONONGA
CHOTERO?

KOMATU
AKUDZOZA
AMBLIYE.

AKADAGULITSIDW
A, NDALAMA ZAKE
NKUZIPEREKA
KWA ANTHU
OSAIKA.

NDI TSITSI LAKE,
MARIYA
ANALIMITSA
MAPAZI A YESU.




MUSIYENI. WACHITA
IZI POKONZEKERA TSIKU
LIMENE NDIDZAIKIDWE
M'MANDA.



AKUTANTHAUZAN
JI PONENA ZA
KUIKIDWA
M'MANDA?

AKUTI
ADZAPACHIKIDWA
PA MTANDA. KOMA
NKUTHEKA KUTI
SAKUNENA ZA
KUKHOMEDWA
KWENIKWENI KUMENE
KUMAPHA ANTHU.



NDAKUUZANI KALE KUTI
MBUSA WABWINO AMATAYA
MOYO WAKE CHIFUKWA CHA
NKHOSA. ANTHU ADZANDIKANA,
ADZANDIPACHIKA PA MTANDA,
NDIPO NDIDZAIKIDWA M'MANDA,
KOMA PA TSIKU LACHITATU
NDIDZAIKANSO.

MARIYA AKUKONZEKERA
KUIKIDWA KWANGA. NTHAWI
YANGA YAFIKA, NTHAWI YOTI
NDILEMEKEZEDWE. TIYENI
TIZIPITA KU YESRUSALEMU
KUMENE ZIMENEZI
ZIDZACHITIKIRE.

MATEYU 20:19;
YOHANE 12:3-8, 10:11



**AMBLIYE,
YERUSALEMU YENSE
AKUDIKIRA KUFIKA
KWANU!**

**PITANI, KANDITENGERENI
BULLU WOTI NDIKWEREPO.
KANO NKOMALIZA KUPITA
KU YERUSALEMU.**



AMBUYE,
ANTHU ZIKWIZIKWI
AKUDIKIRA KULOWA KWANU
MU YERUSALEMU.
AKAKULONGANI UFUMU.

ANTHU ADZANDIKANA
NDIPO ADZANDIPACHIKA
PA MTANDA, KOMA PA
TSIKU LACHITATU
NDIDZAIKA KUMANDA.



MONI,
MFUMU YA
AYUDA.

WODALA
NDIYE AMENE
AKUDZA M'DZINA
LA AMBUYE.


MATAMANDO
AKHALE KWA
MWANA WA
DAVIDE.



IKONZERENI
NJIRA
MFUMU YA
ISRAELE.

MULLINGU
ATAMANDIKE.

MPULUMUTSI
WOLONJEZEDWA.



ANTHU AKUMUTCHA
KUTI MFUMU YA
AYUDA!

AKUGANIZA KUTI
IYEYU NDI MESIYA;
WOLONJEZED


AKUPITIRANJI
KU NYUMBA YA
MULLINGU. AYENERA
KUTI AKUDZIWA TSOPANO
KUTI MOYO WAKE ULI
PA NGOZI?

MWANA WA
DAVIDE,
TIPULLUMUTSENI.



AKUIONGABE
NYUMBA YA MULLINGU.
IKUKHALA NGATI MSIKA
OSATINSO NYUMBA YA
MAPEMPHERO.

NDIKHOZA
KUKUGULITSANI IYI
PA MTENGO WABWINO
KWAMBIRI.
YAVOMEREZEKA KALE
KUTI IKHOZA KUKHALA
NSEMBE.



PEPANI, KOMA
NGATI MUKUFUNA
KUSINTHITSA NDALAMA
MUPITE PENA.
MTENGO
NDAKUPATSANIWU
NDI WABWINO ZEDI.

MATEYU 21:11-12

YESU ANACHITANSO ZIMENE
ANACHITAPO KALE.
ANAYERETSA NYUMBA YA
MULUNGU IMENE
MUNKAKHALA ANTHU AKUBA
NDI ACHIFWAMBA.

CHOTSANI
MALONDA M'NYUMBA
YA ATATE ANGA. NDINU
AKUBA NDIPONSO
ACHIFWAMBA.

MUMABWERA
MUNO NCHOLINGA
CHODZAPEZA NDALAMA
KUCHOKERA KWA ANTHU
OPEMBEDZA. KAGWERENI
KUTALI PAMODZI NDI
NDALAMA ZANUZO.

LIKUGANIZA KUTI
NDIWE YANI?

KHURROO!





ULAMULIRO
WOCHITIRA
ZIMENEZI
WAUTENGA
KUTI?

KHWAAA!


TAONANI!

NYUMBA YA
ATATE ANGA
MUSAISANDUTSE
PHANGA LA ANTHU
ACHIFWAMBA.

AMBUYE, ANSEMBE NDI AFARISI
ATUMA ANTHU OTI ADZAONE ZIMENE
TIKUCHITA. PALI MPHEKESERA ZOTI
AKUPONYANI M'NDENDE CHIKONDWERERO
CHA PASKHA CHISANAYAMBE, NDIYE
KUTI PANGOTSALA MASIKU
OCHEPA KUCHOKERA LEROLI.

NDAKUUZANI KALE KUTI
NDIYENERA KUZUNZIKA
M'MANJA MWAO NDI
KUKHOMEDWA PA MTANDA,
KOMA POTHA MASIKU
ATATU NDIDZAIKANSO.





KODI MUKUDZIWA
TANTHAUZO LOYERETSA
NYUMBA YA MULUNGU
PAMBUYO PAKULOWA MU
YERUSALEMU NGATI
MFUMU?

INDE, UNENERI UMATI
"CHANGU CHA PA NYUMBA YA YEHOVA
CHANDINYEKEZA" NDI KUTI "ADZABWERA
MODZIDZIMUTSA KU KACHISI WAKE."
KUPYOLERA M'ZIMENEZI, YESU
AFUNA KUONETSA KUTI
NDI MESIYA.




TIYENERA KUMUKHALITSA
CHETE CHIKONDWERERO
CHA PASKHA CHISANAFIKE.
TILI NDI KAZITAPE PAKATI
PA OPHUNZIRA AKE.

MASALIMO 69:9;
MATEYU 21:12-13

NDIKUKUCHENJEZANI, INE NDIKAPITA,
ADZAKUPONYANI M'NDEDE,
ADZAKUMENYANI, NDIPO ENA MWA INU
ADZAPHEDWA. MUKACHITIRE LIMBONI KWA
IWO ZA CHIKONDI NDI MPHAMVU ZANGA.
AKADZAKUTENGERANI KU BWALO LA MILANDU,
NDIDZAKUIKANI MALI M'KAMWA MWANU. ANA
ADZATSUTSANA NDI MAKOLO AO, NDIPO
MAKOLO ADZATSUTSANA NDI ANA AO. ANTHU
ADZADANA NANU CHIFUKWA CHOTI
MUMANDIDZIWA. ANENERI ONYENGA AMBIRI
ADZAONEKA NDIPO AZIDZANAMA KUTI
AKUNENERA M'DZINA LANGA. MZIMU
WOYERA ADZAKHALA NANU.





AMBUYE, KODI
CHIZINDIKIRO CHA
KUBWERANSO KWANU
NDI NYENGO YA KUTHA
KWA DZIKO LINO
CHIDZAKHALA CHIYANI?




WINA AKADZATI INE NDIKUBWERA PA NTHAWI YAKUTIYAKUTI, KAPENA KUTI NDILI KU MALO ENA, MUSADZAMKHULLUPIRIRE WOTEROYO, POPEZA NDIDZABWERA NGATI MMENE CHIMACHITIRA CHING'ANING'ANI. KHALANI OKHULLUPIRIKA KWA INE, NDIPO PAMAPETO PAKE MUDZAPULUMUKA KU MKWIYO UMENE UDGAGWERA ANTHU OCHIMWA. CHONCHO KHALANI TCHERU, POPEZA SIMUDZIWA TSIKU KAPENA NTHAWI IMENE NDIDZABWERENSOYO.






MONGA MOMWE ZINALILI PA MASIKU
A NOWA, ZIDZAKHALANSO CHIMODZIMODZI
PAMENE NDIDZAKHALA PAFUPI KUBWERA. ANTHU
ANATANGWANIKA NDI ZOSANGALATSA ZA MOYO
UNO NDIPO SANAZINDIKIRE MPAKA CHIGUMULA
CHINAWAPEZA NDI KUWASESA ONSEWO.
NDIDZABWERA MODZIDZIMUTSA MONGA
MOMWE MBALA IMABWERERA USIKU.



ANTHU AWIRI
AZIDZAGWIRA NTCHITO
M'MUNDA. WINA
ADZATENGEDWA KUTI
AKAKUMANE NANE NDIPO
WINAYO ADZATSALA
KUTI AZUNZIKE.

AMAI AWIRI AZIDZASINJA PAMODZI PA
MTONDO. WINA ADZATENGEDWA KOMA
WINAYO ADZATSALA. INUYO MUNGOKHALA
TCHERU NDI KUMAKONZEKERATU, POPEZA
NDIDZABWERA PA TSIKU LIMENE
SIMUKUYEMBEKEZAKO.



AMBUYE, NDIFUNA
NDIKAONE MUNTHU
WINA MUMZINDAMU.
NDIKUPEZANI
NTHAWI INA.

YUDASI, PITA,
NDIPO UKACHITE
ZIMENE UKUFUNA.



MUTANDIPATSA
NDALAMA
ZOUCHULUKIRAPO NDITHU,
NDIKHOZA KUMUPEREKA
YESU M'MANJA
MWANU.

KODI SINDIWE
YUDASI, MMODZI
MWA OPHUNZIRA
AKE?

INDE, NDIPO NDAKHALA
NAYE KWA ZAKA ZITATU, KOMA
NDATOPA NAZO ZIMENE
AMAPHUNZITSA. AKUYANKHULA NGATI
MUNTHU WOZEREZEKA, NDIPO INE
NDIKUFUNA NDALAMAZO KUTI
NDIGWIRITSE NTCHITO.

NTHAWI YAKWANA
KUTI NDILEMEKEZEDWE.
MBEU YA TIRIGU
IKAPANDA KUGWA
M'NTHAKA NDI KUFA,
IMANGOKHALA BASI,
KOMA IKAFU IMABALA
TIRIGU WAMBIRI.




MATEYU 26:14-16; MARKO 13:5-13; LUKA 17:26-37;
YOHANE 12:23-24; 2 PETRO 3:10

**MOYO WANGA TSOPANO UKUSALTSIDWA.
KODI NDINENE KUTI, "ATATE, MUNDIPULUMUTSE KU
NTHAWI IYI"? AI, CHIFUKWA INE NDINABWERA PA
DZIKO LAPANSI CHIFUKWA CHA NTHAWI IMENEYI.**





ATATE,
LEMEKEZANI
DZINA LANU.



**NDALILEMEKEZA
KALE DZINA
LANGA NDIPO
NDIDZALILEMEKEZ
ANSO.**

**NDIPO
KUYANKHULAK
O KUNAMVEKA
NGATI BINGU.**


**MULLINGU
WAYANKHULA
NAYE!**

**MNGELO
ANAYANKHULA
NAYE!**

**LIU LIMENE MWAMVALO
SILINABWERE CHIFUKWA CHA INE,
KOMA CHIFUKWA CHA INLYO.
NTHAWI YAFIKA TSOPANO PAMENE,
WOLAMULIRA WA DZIKO LINO,
SATANA, AONONGEDWE. NDIPO
NDIKAKHOMEDWA PA MTANDA KUTI
NDIFE, NDIDZAKOKERA ANTHU
ONSE KWA INE MWINI.**

**IFE TIMADZIWA
KUTI MNENERI ADATI
MESIYA SADZAFI
KONSE, NDIPO INU
MUKUTI MUKUFA;
KODI NDIYE KUTI
MESIYA NDANI?**





KUWALA KUDZAKHALA NANU
KWA KANTHAWI KOCHAPA CHABE.
KHULUPIRIRANI KUWALAKO
PAMENE MULI NAKO, KUTI TSONO
MUKHALE ANA A MULLINGU.

NDIKLONA
NGATI
ZOZELEZEKA
ZIMENEZI.



MUNTHU AKAKANA INE PAMODZI NDI MAU ANGAWA, NDIYE KUTI AKUKANA MULLINGU. INE NDINE KUUNIKA KWA DZIKO LAPANSI. MUKANDIKHULLUPIRIRA SIMUDZAKHALA MU MDIMA, KOMA MUDZAKHALA NDI MOYO WOSATHA.

YOHANE 12:27-36



<https://goodandevilbook.com/>